Kalata ya No. 52

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitso kuchokera m'Baibulo kupita kwa amene akulalikira Uthenga Wabwino

KASANU NDI KAWIRI

Pamapeto pa ulendo wautali ndi wotopetsa wa zaka zokwana 40 akuyendayenda m'chipululu atachoka ku Igupto, pomaliza Aisraele pomalizira anafika ku Dziko Lamalonjezano. Awa amene kale anali akapolowo anaoloka mtsinje wa Yordano nalowa mdziko lawo latsopano. Chikhulupiriro chawo ndi kumvera kwawo zinayesedwa mobwerezabwereza, kuti iwo aphunzire kumudalira Mulungu. Iwo anali atakumana ndi zowawa zambiri, kukaikira ndi kusakhulupirira koma potsirizira pake, mwa chisomo cha Mulungu, iwo anafika ku dziko loyenda mkaka ndi uchi. Dziko lokongolali limene analakalaka kuliona kwa zaka zambiri linalinso ndi mizinda yotchingidwa ndi mipanda komanso ziphona.

Aisraele anafika kumzinda wa Yeriko wokhala ndi mipanda yolimba kwambiri. Ngakhale kuti zinkaoneka ngati ndi zosatheka kugonjetsa mzinda woterowo, Mulungu sanawasiye iwo ku luso lawo ndi malingaliro awo. Mulungu anauza Yoswa kuti, "Ndapereka Yeriko m'manja mwako" (Yoswa 6:2). Mulungu anapatsa Yoswa malangizo achindunji kuti azungulire mzindawo kamodzi pa tsiku kwa masiku 6, ndipo pa tsiku la 7 awuzungulire mzindawo kokwananso ka 7. Pamene akuzungulira mzindawo ka chi 7, ansembe adzalize malipenga awo, anthu adzafuule ndi kufuula kwakukulu, ndipo malinga a mzindawo adzagwa.

Aisraele anamvera lamulo la Mulungu ndipo anaguba mwakachetechete tsiku ndi tsiku. Kukhala chete kwawo kunali koposa kumvera, popeza kunaonetsa kupembedza ndi chikhulupiriro mu pulani ya Mulungu. Tsiku la 6 silinkasiyana ndi loyamba lija, popeza palibe chomwe chinachitika, ndipo zobwerezabwereza zija zinkaoneka zopanda phindu. Kulimbikira kwawo kunafika pachimake pa tsiku la 7, pamene chikhulupiriro ndi kumvera kwawo zinabala zipatso. Pamene malipenga anali kulira ndipo anthu akufuula, chosatheka chinachitika popeza makomawo anagwa. Mzindawo unagonjetsedwa, ndipo zinthu zinayenda bwino kwambiri. Ngakhale kuti malangizo a Mulungu aja samapezeka mu mabuku onena za kamenyedwe kankhondo, Aisraele ankadalira Mulungu. Chikhulupiriro chawo chosagwedera ndi kumvera Mulungu kwawo kunabweretsa chipambano.

Lingaliro la kumvera limapezeka m'Malemba onse. Mulungu akuitana anthu ake kuti akhale ndi chikhulupiriro ndi kumvera pulani yake laumulungu. Nthawi zambiri malangizo a Mulungu samagwirizana ndi malingaliro aumunthu, koma anthu akagonjera Mulungu,amapeto ake amapeza kuti cholinga cha Mulungu, nthawi yake, ndi mphamvu zake zili zangwiro. Ngakhale palibe chomwe chachitika patapita masiku 6, miyezi yokwana 6, kapena zaka zokwana 6, khalani osasunthika pakumvera. Mulungu akakhala chete sizitanthauza kuti Iyeyo palibepo. Kawirikawiri kudikira, komanso kumvera kobwerezabwereza, ndi zimene zimasula chikhulupiriro chathu, ndipo zofuna za Mulungu zimavumbulitsidwa. Tsiku la 7 lidzafika.

Nambala ya 7 mu Baibulo imaimira kukwaniritsidwa ndi ungwiro waumulungu. Pamene malangizo a Mulungu akumatsutsa kumvetsetsa kwathu ndipo sakugwirizana ndi zimene timakonda, tiyeni tikhalebe okhulupirika ndi omvera ndi kuwatsatirabe mpaka kokwana ka 7, kapena mpaka pamene cholinga cha Mulungu chitakwaniritsidwa. Monga mmene Aisraele anamvera malangizo a Mulungu ku Yeriko, nkhani ina ya kumvera ikuchokera pa moyo wa Namani.

(Yapitirira pa tsamba 2)

"Kawirikawiri mu kudikira, ntchito zobwerezabwereza za kumvera, mmene chikhulupiriro chathu chimasulidwa, ndipo zofuna za Mulungu zimavumbulitsidwa."

Mau a Mkonzi	Kalozera pophunzira Baibulo: Kumvera	Moyo Womvera	Funso Yanko	Mau a Nyengo Yake: Lalikira Mau
3	4	5-6	7	8

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu
2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi
Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa
Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano
Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4; Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo
1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera
Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero
Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16; Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu
Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo
Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13; Akol. 1:18

Umodzi
Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti
Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30; 1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso
Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja
Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3; 1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena
1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza
2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10; Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere
Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza
Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino
Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

Namani, kazembe wamkulu ndi wamphamvu wa Asiriya, anali ndi khate. Atapempha kuti amuchiritse, mneneri Elisa anatumiza mau kwa Namani kuti akasambe mumtsinje wa Yordano kokwana ka 7. Pa Mafumu 5:10-14 amafotokoza kuti Namani anakwiya kwambiri chifukwa chakuti kumizidwa mumtsinje wamatope kunali chinthu chachilendo ndi chachikunja. Iye ankayembekezera chinachake chochititsa chidwi kwambiri monga kuthiridwa madzi mwamphamvu pofuna kuti alandire chozizwitsa. Koma atapemphedwa ndi anyamata ake, Namani anadzichepetsa nachita zimene anamulangiza. Atasamba mu mtsinje wa Yordano kokwana ka 7, thupi lake linakonzeka, ndipo anayeretsedwa.

Nthawi zambiri njira za Mulungu zimasemphana ndi ziyembekezo za anthu. Kumvera nkofunika kwambiri ngakhale pamene tikuona kuti nkosafunika kapena ngati sitikufuna kumvera basi. Pamene Namani anadzichepetsa, anapeza machiritso ochokera kwa Mulungu—osati mwa madzi enieniwo koma chifukwa chofunitsitsa kukhulupirira ndi kuchita mogwirizana ndi mau a Mulungu.

Chitsanzo china ndi Eliya chikusonyeza phunziro ili. Chilala chitatenga nthawi yaitali, Eliya anapemphera ndi chikhulupiriro kuti mvula igwe. Anatumiza wantchito wake kuti ayang'ane kunyanja kuti akaone chizindikiro cha mvula. Nthawi zonse, wantchitoyo ankabwera nkunena kuti: "Kulibe kalikonse" (1 Mafumu 18:43-44). Eliya anapitiriza kupemphera ndipo wantchitoyo atakayang'ana kokwana ka 6, palibe chimene chinasintha popeza kuthambo kunali koyera.

Eliya, ndi chikhulupiriro chosagwedera, anapitiriza kupemphera. Anatumiza mnyamatayo kuti akayang'ane kunyanja kachi 7 ndipo anabwera ndi mau akuti: "Pali mtambo waung'ono wofanana ndi dzanja la munthu." Eliya anatumiza uthenga kwa Mfumu Ahabu womuuza kuti akonzere mvula imene inali pafupi kugwa. Kumwamba "kunada ndi mitambo, ndipo kunagwa mvula yamphamvu." (1 Mafumu 18:45) Kumwamba kunachita mdima wa bii. Kodi Eliya akanasiya kupemphera pa ulendo wa chi 6? Mulungu sagwira ntchito pa nthawi yathu, koma amafuna kuti tizipempherabe.

Kugwa kwa Yeriko, kuchiritsidwa kwa Namani ndi mvula zonse zinachitika pambuyo pa maulendo okwana 7. Ngakhale kuti nambalayo ndi yophiphiritsa, ikuimiranso nthawi yangwiro ya Mulungu. Mphamvu ya Mulungu inaonekera pamene kumvera ndi chikhulupiriro zinagwira ntchito. Ngakhale mu nthawi ya kutopa, kukhumudwa kapena kukaika, tiyenera kukhulupirira zolinga za Mulungu ndi kumumvera mokwanira, kuposa mmene tingamve kapena kuona. Pamene tikukumana ndi mavuto m'miyoyo yathu, tiyeni tipitirirebe m'chikhulupiriro, kukhulupirira malonjezo a Mulungu. Tisaleke pa 'nthawi ya chi 6' koma tilimbikire, kaya m'pemphero, kukhulupirira, kumvera podziwa kuti nthawi yachi 7 ya Mulungu ndi yolondola nthawi zonse. Ngakhale mudikire kwanthawi yaitali bwanji kapena ulendowu ndi wovuta bwanji, khulupirirani kuti dongosolo la Mulungu ndi langwiro. Cholinga chake chidzakwaniritsidwa tikakhala okhulupirika ndi omvera. ■

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani. —Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi

Ngati musunga malamulo anga mudzakhala m'chikondi changa; monga Ine ndasunga malamulo a Atate wanga, ndipo ndikhala m'chikondi chake. — Yohane 15:10

Chinsinsi cha kukhalabe mu ubale wachikondi ndiko kuyang'ana moposera pa zilakolako zathu zaundekha ndi kulingalira komanso kulemekeza zosowa ndi zokhumba za munthu wina. Yesu anatiphunzitsa zokhudzana ndi chifuniro cha Atate pa miyoyo yathu ndipo anati ngati tisunga malamulo ake, tidzakhazikika m'chikondi chake. Palibenso malo otetezeka kuposa m'chikondi cha Mulungu.

Anthu amafuna malo othawirako, mtendere ndi chiyembekezo zochokera kwa Mulungu, koma ndi owerengeka okha amene amakwaniritsa gawo lawo la ubalewu. Ngati tikufunadi kuona chikondi cha Mulungu ndi malonjezo onse amene amabwera nawo, tiyenera kusunga malamulo ake.

Mutu wathu ulendo uno ndiwo "Kumvera." Tiyenera kunena kuti "ayi" kwa ife eni ndipo "inde" kwa Mulungu. Tikafuna kutsatira maganizo athu ndi zimene timakonda, tiyenera kuima ndi kulola kuti chifuniro cha Mulungu chichitike. Mulungu akufunafuna anthu amene adzakhala omvera gawo lililonse la moyo. Sitingakondweretse Mulungu ngati tisankha ndi kulola magawo amene ifeyo timvere. Nkosavuta kudzilungamitsa pa kusamvera kwathu mu gawo limodzi posonyeza kumvera kwathu mu gawo lina. Tikuyenera kumvera choonadi chonse.

Mukafuna kutipeza pa intaneti, mulembe www.thegospeltruth.org kuti mudzilandira makalata athu kapenanso kuti muone makalata akale.

Zimene Baibulo limaphunzitsa zenizeni ndipo palibe kuzitsutsa, koma kumvera ndiko kusankha kwathu. Ndi chinthu chimodzi kuyang'ana ochimwa ndikuwona miyoyo yawo ya kusamvera. Ndi chinthu chinanso kudzifufuza tokha komanso mipingo yathu. Kodi tikukhala mu kumvera kotheratu kwa Mulungu? Kodi tikulankhula, kuchita, kukhala ndi moyo, kuvala, ndi kuchita zinthu mogwirizana ndi choonadi chonse chimene timachidziwa ndi kumvetsa? Tiyeni tifunse kuti, "Ambuye, mukufuna kuti ndichite chiyani?"

Kumvera kumaposa Mau olembedwa a Mulungu. Mzimu wa Ambuye amatiwongolera ndi kutitsogolera mu choonadi. Iye amatsutsa komanso kulangiza. Kodi tikuchita chiyani kwa Mzimu? Kodi timadzipereka mwachangu ku zotitsutsa zing'onozing'ono za Mzimu? Ngati sichoncho, chikumbumtima chathu chidzazilala, ndipo tidzapitirira kukhala osasamala komanso osalabadira ntchito ya Mzimu mu miyoyo yathu.

Ngati tisiya kuchita changu pa kumvera, kumakhala kovuta kwambiri kubwerera ku malo amene tikhoza kumvera mosamala ndi kotheratu pakuyenda kwathu ndi Mulungu. Kusamvera ku gawo limodzi la moyo kumathamangira kupita ku magawo ena a moyo wathu. Malo omwe tidapambanapo kale ndi Mulungu adzayamba kusautsika chifukwa cha kusamvera komwe kwapezeka ku gawo lina.

Tiyeni tikhale tcheru ku zimene Mzimu akuchita ndipo tifulumire kumvera zochita za Mulungu m'miyoyo yathu.

Michael W. Smith

April 2025

Kutumikira Ambuye ndiko kumvera kosavuta:

> kupita kumene Mulungu akufuna kuti tipite,
> kuchita zomwe Iye akufuna kuti tichite,
> kulankhula monga Iye akufuna kuti ife tilankhule.



Kalozera Pophunzira Baibulo

Mutu: Kumvera

Mau a Mulungu: *Ngati mukonda Ine, sungani malamulo anga.*— Yohane 14:15

Tanthauzo: Kumvera ndiko khalidwe kapena mchitidwe wa kumvera. Kumaphatikizapo kutsata lamulo, pempho, langizo, kapena kugonjera ku ulamuliro wa wina. (*Zinenero za Oxford*).

Mwachidule: Pali kugwirizana kwakukulu pakati pa kukonda Mulungu ndi kumvera Mau ake. Kumvera Mau a Mulungu ndi kutsatira chitsogozo cha Mzimu ndikofunikira kuti tikhale ndi moyo waumulungu. Kumvera kumabweretsa madalitso ndipo pamapeto pake moyo wosatha, pamene kusamvera kumadzetsa kutaya ndi kulekanitsidwa kwamuyaya ndi Mulungu.

I. Kuitanidwa kuti timvere

A. Deuteronomo 11:1 Sungani malamulo a Mulungu nthawi zonse.
B. Yohane 14:15 Sungani malamulo anga.

II. Kulimbikitsa kuti timvere

A. Yohane 14:23 Ngati munthu akonda ine.
B. Yohane 14:24 Iye wosakonda Ine.

III. Ziphunzitso za Yesu

A. Mateyu 7:24-27 Munthu wanzeru ndi wopusa.
B. Luka 6:46 Munditchuliranji Ine Ambuye, koma osamvera?
C. Mateyu 21:28-31 Fanizo la ana aamuna awiri.

IV. Kugonjera ndi kukhulupirira Mulungu

A. Yakobo 4:7 Dziperekeni kwa Mulungu.
B. Luka 22:41-42 Osati chifuniro changa, koma chanu.
C. Miyambo 3:5-6 Khulupirirani Ambuye.

V. Madalitso pa kumvera

A. Eksodo 23:22 Mulungu adzateteza.
B. Yesaya 1:19 Idyani zabwino za dziko.
C. Machitidwe 5:32 Mzimu Woyera unaperekedwa kwa omvera.
D. Yohane 8:51 Omvera adzakhala ndi moyo wosatha.

VI. Zitsanzo za kumvera

A. Yesu: Afilipi 2:8 Womvera kufikira imfa.
B. Abrahamu: Genesis 22:1-18 Wololera kupereka nsembe.
C. Paulo: Machitidwe 26:19 Anamvera maitanidwe ake.
D. Nowa: Genesis 6:14, 22 Anachita zonse zimene Mulungu analamula.

VII. Zotsatira za kusamvera

A. Duteronomo 8:20 Osamvera adzaonongeka.
B. 2 Atesalonika 1:8 Kubwezera chilango kwa iwo osamvera Uthenga Wabwino.
C. Aefeso 5:5-6 Iwo sadzalowa mu ufumuwo.

VIII. Zitsanzo za kusamvera

A. Adamu ndi Hava: Genesis 3:3-6 Tchimo loyamba la kusamvera.
B. Sauli: 1 Samuele 15:3-23 Kumvera kuli bwino kuposa nsembe (v22).
C. Mneneri wosamvera: 1 Mafumu 13:26 Anaphedwa ndi mkango.
D. Yona: Yona 1:1-3 Anathawa Mulungu.
E. Israele: Yeremiya 6:16 Sitidzayendamo mmenemo.

IX. Kukhala monga ana omvera

A. 1 Petro 1:13-14 Khalani ngati ana omvera.
B. 1 Yohane 3:24 Iye amene asunga malamulo a Mulungu akhala mwa Iye.
C. Aefeso 2:2 Ana a kusamvera.

X. Kuphunzitsa ndi kusunga kumvera

A. Mateyu 28:19-20 Aphunzitseni kusunga zinthu zonse.
B. 2 Akorinto 2:9 Khalani omvera mu zonse.
C. Machitidwe 5:29 Mverani Mulungu koposa anthu.

XI. Kumvera mu zochita

A. Aroma 6:16 Inu ndinu akapolo amene mumamvera.
B. (Salmo 119:59-60) Davide anamvera mofulumira.
C. (Ahebri 2:1-3) Samalani kuti tisalole kuti Mau a Mulungu apulumuke.

Kumaliza

Pakuti ichi ndi chikondi cha Mulungu, kuti tisunge malamulo ake: ndipo malamulo ake sali olemetsa. — 1 Yohane 5:3

Moyo womvera

Kusankha njira ya Mulungu ya moyo wa madalitso ndi mphotho yamuyaya.

Kodi kukhala ndi moyo womvera kumatanthauza chiyani? Kuyambira pachiyambi penipeni, Mulungu analenga anthu kuti azidzisankhira zochita. Mphamvu iyi yosankha imene imawapanga anthu kukwanitsa kuonetsa chikondi. Kumvera, kumene kuli kusankha njira ya Mulungu koposa yathu, ndiko umboni komanso chipatso cha chikondi chenicheni.

"Kumvera sikutanthauza mantha kapena ukapolo koma ndi chipatso chachibadwa cha chikondi chenicheni kwa Mulungu."

Kufunika kwa kumvera

Ngati tikufuna kutumikira Mulungu ndi kulandira moyo wosatha, tikuyenera kukhala ndi moyo womumvera Iye. Anthu ambiri amafuna kutsata zilakolako za iwo eni, zimene zimasemphana ndi Mau a Mulungu. Mulungu anapereka dongosolo lodabwitsa kudzera mwa Mwana wake, Yesu Khristu, komanso kudzera m'Malemba. Pokhala Mlengi wathu, dongosolo la Mulungu ndi cholinga chake pa miyoyo yathu zidzabweretsa mtendere ndi kukwaniritsidwa kwakukulu. Komabe, tiyenera kudzikaniza tokha, tigonjere, ndi kuvomereza kwathunthu malangizo ndi utsogoleri waumulungu. Kodi mukukhala mu kumvera chifuniro cha Mulungu pa moyo wanu?

Kusamvera koyamba

Mulungu anaika mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoipa m'munda wa Edeni. Iye anauza Adamu ndi Hava kuti: "Usadye umenewo; chifukwa tsiku lomwe udzadya umenewo udzafa ndithu" (Genesis 2:17). Mulungu amafuna kuti pakhale ubale wachikondi ndi chilengedwe chake, ndipo mtengo umenewo ndi umene unapatsa Adamu ndi Hava mphamvu yosankha mmene ankafunira kukhalira moyo. Asanachite kusamvera, ankasangalala ndi moyo wochuluka monga momwe Mulungu ankafunira. Poganiza kuti akudziwa bwino, iwo sanamvere, zomwe zinabweretsa imfa yauzimu ndi yakuthupi. Momwemonso, tikasokera pa dongosolo la Mulungu mu kusamvera, timadzikhalitsa kutali ndi kupezeka kwake m'moyo uno komanso uli mkudzawo.

Kumvera ndi chizindikiro cha chikondi chenicheni

Monga momwe Adamu ndi Hava anapatsidwa malamulo aumulungu, momwemonso ana a Israele anapatsidwa malamulo. Iwo analangizidwa kuti nthawi zonse asunge malamulo a Mulungu, malemba, maweruzo, ndi malamulo (Deuteronomo 11:1). Yesu anati pa Yohane 14:15, "Ngati mukonda Ine, sungani malamulo anga." Kusunga malamulo ndi kutsatira chitsogozo cha Mzimu zili zofunikira pakukhala moyo wachikhristu. Anthu ambiri amavomereza Khristu ndi pakamwa pawo, koma zochita zawo zikutsutsana ndi umboni wapakamwa. Yesu anafunsa kuti, "Ndipo munditchuliranji Ine, Ambuye, Ambuye, ndi kusachita zimene ndizinena?" (Luka 6:46).

Kodi chimakutakasani ndi chiyani?

Kumvera sikutanthauza mantha kapena ukapolo koma ndi chipatso chachibadwa cha chikondi chenicheni kwa Mulungu. Yesu anaphunzitsa momveka bwino mu Yohane 14:23-24 kuti ngati wina amukonda Iye, adzasunga mau ake. Iwo amene samukonda Iye sadzasunga zonena zake. Ngakhale kuti chiphunzitsochi chikuoneka ngati chophweka, chimaulula zenizeni zimene amakumana nazo anthu ndi Mulungu.

Munthu wanzeru ndi wopusa

Yesu anaphunzitsa kuti anthu amene amamva zimene iyeyo ankaphunzitsa nkuzitsatira adzakhala ngati munthu wanzeru amene anamanga nyumba yake pamaziko olimba. Iye anayerekezera anthu amene anamva Mau koma osawachita ndi munthu wopusa amene anamanga nyumba yake pamchenga. Namondwe atabwera, nyumba ya munthu wanzeruyo ndi imene inaima njii. Kusankha kwathu ndi kumene kutipangitse kukhala anzeru kapena opusa.

Vuto logonjera

Kumvera kumatanthauzidwa kutsatira malangizo ndi kugonjera ulamuliro wa wina. Mkhristu woona ayenera kumvera chifuniro cha Mulungu. "Potero

(Yapitirira pa tsamba 6)

(Kuchokera pa tsamba 5)

mverani Mulungu" (Yakobo 4:7). Kumvera Mulungu kumafuna kudzipereka tokha ndi kukweza chifuniro chake pamwamba pa chifuniro chathu. Anthu ambiri odzitcha Akhristu sanapereke moyo wawo, maloto, ndi zolinga zawo kwa Mulungu. Ngakhale kuti nthawi zina zimakhala zovuta, koma kudzera mu kumvera kotheratu kumene timapeza mtendere waukulu kwambiri.

Kudalira kumatsogolera ku kumvera

Miyambo 3:5-6 imapereka malangizo abwino kwambiri ndipo imayala maziko abwino a kumvera. "Khulupirira Yehova ndi mtima wako wonse, osachirikizika pa luntha lako; umlemekeze m'njira zako zonse, ndipo Iye adzaongola mayendedwe ako." Tikaphunzira kudalira Ambuye m'malo modalira nzeru zathu, kumvera kumakhala kosavuta.

"Ngati timvera chiphunzitso cha Khristu, tidzapeza moyo wosatha ndi kusangalala ndi madalitso a Kumwamba."

Madalitso adzatsatira

Kumvera Ambuye kumabweretsa madalitso a Mulungu m'moyo uno komanso wa mtsogolo. "Odala iwo akumva mau a Mulungu, nawasunga" (Luka 11:28). Mneneri Yesaya analengeza kuti: "Ngati inu muli ofuna ndi omvera, mudzadya zabwino za dziko" (Yesaya 1:19). Choncho uku sikuli kumvera mokakamizidwa koma kumvera mwaufulu motsogozedwa ndi chikondi. Yesu anaphunzitsa ophunzira ake kuti, "Munthu akasunga mau anga, sadzaona imfa nthawi yonse" (Yohane 8:51). Iye anali kunena za imfa yamuyaya. Ngati timvera chiphunzitso cha Khristu, tidzapeza moyo wosatha ndi kusangalala ndi madalitso a Kumwamba.

Zitsanzo za kumvera

M'Baibulo muli zitsanzo zolimbikitsa za anthu amene ankamvera Mulungu. Abrahamu anachoka kumudzi kwawo osadziwa kumene amapita, chifukwa chakuti amamvera kuitana kwa Mulungu. Pa kumvera kwa nthawi yomweyo, iye anadzuka m'mamawa, nalolera kupereka mwana wake nsembe kwa Mulungu (Genesis 22:1-18). Paulo, woitanidwa kukatumikira uthenga wabwino, anati, "Sindinakhale ine wosamvera masomphenya a Kumwamba" (Machitidwe 26:19). Nowa, mosasamala kanthu za kunyozedwa anasutsa maganizo a anthu ndipo, anachita "monga mwa zonse anamlamulira iye Mulungu" (Genesis 6:22) pamene anamanga chingalawa. Kumvera kumeneko kunakhala chipulumutso chake, monga momwe zidzakhalirenso ndi ife. Khristu mwini "anakhala womvera kufikira imfa" (Afilipi 2:8). Kumvera kumeneko kunabwera ndi mtengo waukulu. Iye anapereka chitsanzo pamene anapemphera kuti: "Atate, mukafuna Inu, chotsani chikho ichi pa Ine; koma si kufuna kwanga ai, komatu kwanu kuchitike." Mpaka tipemphera pemphero ngati lmeneli, sitidzapeza chisomo chonyamula mtanda wathu ndikupeza chiukitsiro chaulemerero.

Zotsatira za kusamvera

Kwa iwo amene amasankha kusamvera Ambuye m'zinthu zonse, palinso zotsatira zake. Mulungu anauza Aisraele kuti: "momwemo mudzaonongeka; chifukwa cha kusamvera mau a Yehova Mulungu wanu" (Duteronomo 8:20). Paulo anatchula zina mwa zinthu zosalungama ndipo anapereka chenjezo lalikulu lakuti: "Asakunyengeni inu munthu ndi mau opanda pake, pakuti chifukwa cha izi umadza mkwiyo wa Mulungu pa ana a kusamvera" (Aefeso 5:5-6). Kusamvera kumatsogolera ku imfa yamuyaya. Kodi phindu lake lidzakhala lotani kukhala ndi moyo molingana ndi thupi komanso kutsatira zilakolako zathu ndi kukathera ku gehena?

Kumvera kumaposa kupereka nsembe

Chiweruzo cha Mulungu chinachititsa Mfumu Sauli kutaya ufumu wake chifukwa cha kusamvera. Mau a pa 1 Samuele 15:1-23 amafotokoza nkhani yomvetsa chisoni ya Sauli amene anauzidwa kuti aononge ziweto zonse za Aamaleki pambuyo pa nkhondo. Sauli anasiya zina nkuzipereka nsembe kwa Mulungu. Mneneri Samuele atafika, anafunsa kuti: "Koma tsono kulirako kwa nkhosa ndilikumva m'makutu anga?" Samuele anauza Sauli kuti: "kumvera ndiko kokoma koposa nsembe." Mulungu anakana Mfumu Sauli, monga mmene iye adzakanire anthu osamumvera. Zowiringula zonse, kulungamitsidwa, ngakhalenso nsembe sizitanthauza kanthu pakakhala kusamvera.

Zitsanzo za kusamvera

Malemba ali odzaza ndi zitsanzo zina zoyenera kuphunzira: mneneri wosamvera wa pa 1 Mafumu 13 amene anapatuka pa malangizo a Mulungu anaphedwa ndi mkango; ndipo Yona, amene anathawa kwa Mulungu, anapezeka m'mimba mwa chinsomba. Kusamvera sikwabwino.

Kukhala mu kumvera

Ambuye amatiitana kuti tikhale "monga ana omvera" (1 Petro 1:14) ndi kukhala mwa Iye (1 Yohane 3:24) mwa kusunga malamulo ake. Yesu anatumiza ophunzira ake ndi ntchito yakuti: "Phunzitsani anthu amitundu yonse…ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulani inu" (Mateyu 28:19-20). Kumvera pang'ono sikokwanira. Tiyenera kukhala "omvera m'zonse" (2 Akorinto 2:9). Pamene zopsinja ndi zotikopa zimatilimbikitsa kuchita zoipa, "Tiyenera kumvera Mulungu koposa anthu" (Machitidwe 5:29).

Kudzifufuza

"Amene mudzipereka eni nokha kukhala akapolo ake akumvera iye, mukhalatu akapolo ake a yemweyo" (Aroma 6:16). Kodi ife tikumvera ndani? Ndife atumiki a ndani? Tiyeni tinene kuti "ayi" kwa ife tokha ndikudzipereka tokha kwa Mulungu. Tiyeni, monga Davide, tilingalire njira zathu ndi kutembenuzira mapazi athu ku maumboni a Mulungu. Davide anati "Ndinafulumira, osachedwa, kusamalira malamulo anu" (Salmo 119:59-60). Kodi ndife omvera m'zinthu zonse? Ngati timakonda Mulungu, tiyeni tizisunga malamulo ake, chifukwa "malamulo ake sali olemetsa" (1 Yohane 5:3). Ndiwo njira yopezera madalitso, mtendere, ndi moyo wosatha. ■

Funso ? Yankho

Kodi lemba la Ahebri 5:8 limatanthauza chiyani likamanena kuti Yesu “anaphunzira kumvera”?

Pa Ahebri 5:8-9 amanena kuti: “Ngakhale kuti anali Mwana, anaphunzira kumvera ndi zowawa zimene anakumana nazo, ndipo pamene anapangidwa kukhala wangwiro, anakhala woyambitsa wa chipulumutso chosatha kwa onse amene amamumvera.”

“Kuphunzira kumvera” sikutanthauza kuti Yesu anali wosamvera kapena kuti sankazindikra zokhudza kumvera. Yesu Khristu anali wangwiro mwauzimu ndi mwamakhalidwe. Komabe, Yesu anatengera mbeu ya Abrahamu ndipo anabwera ku dziko lapansi m’thupi. Anakumana ndi mayesero, kukanidwa, chisoni, ndi zowawa kuti akhale mkhalapakati woyenerera pakati pa munthu ndi Mulungu.

Yesu, monga Mulungu ndi munthu, anaonetsera kumvera m’zochita zake kupyolera m’zokumana nazo zake zaumunthu. Ali padziko lapansi, Yesu anamvera makolo ake a padziko lapansi ndiponso Atate wake wakumwamba. Kumvera kumeneko sikunali kopanda kulimbana m’thupi. Yesu anapemphera kuti ngati n’kotheka, chikho cha masautso chichotsedwe; komabe Iye monga munthu mu thupi anadzipereka ku chifuniro chaumulungu cha Atate.

Afilipi 2:8 imawonjezera kumvetsetsa kwathu kuti: “Ndipo popezedwa m’maonekedwe ngati munthu, anadzichepetsa yekha, nakhala womvera kufikira imfa, ndiyo imfa ya pamtanda”. Kunali kumvera kudzera mu chidziwitso ndi kuonetsa pochita.

Yesu anadzipereka yekha ku imfa ya pamtanda monga nsembe yangwiro. Ntchito yake monga mlembi wa chipulumutso inakhala yangwiro, kapena kuti inatsirizidwa, pamene Iye anafa ndi kuukanso. Makamaka, Yesu “anaphunzira kumvera” mwa kukhala ndi moyo ndi kuvutika m’thupi pamene anali wodzipereka kotheratu kwa Mulungu ngakhale mu imfa. ■



Kukulitsa kumvera kwaumulungu

Mmene kumvera makolo kumatsogolerera kumvera Mulungu.

M’dziko lamakonoli, mmene kusamvera ndi kunyozera ulamuliro kumaonekera ponseponse, kukulitsa kumvera kwaumulungu kwa ana n’kofunika kwambiri kuposa kale lonse. Chimodzi mwa zizindikiro za masiku otsiriza, monga momwe chanenedwera pa 2 Timoteo 3:1-2, ndicho ana kukhala “osamvera akuwabala.” Kusamvera kumeneku nthawi zambiri kumasonyeza kusamvera Mulungu kwa anthu ambiri.

Makolo amathandiza kwambiri kuti ana awo aziyenda bwino mwauzimu. Pa Aefeso 6:4 amalimbikitsa makolo kulera ana awo “m’maleredwe ndi chilangizo cha Ambuye.” Kulera kumeneku kumayamba ali aang’ono, kuphunzitsa ana kufunika kwa mau akuti “AYI”. Ana akaphunzira kulemekeza ndi kumvera makolo awo, amakhala ndi maziko olemekeza ndi kumvera Mulungu.

Ulemu ndi kumvera zimayenera kukhazikitsidwa m’nyumba. Mwana amene amaphunzira kulemekeza ulamuliro wa makolo samavutika kulemekeza maulamuliro ena, kuphatikizapo Mulungu. Kuphunzitsa ndi kupereka chilango zikuyenera kuchitidwa mwachikondi ndi mosasinthasintha, ndi cholinga cholimbikitsa makhalidwe abwino ndi makhalidwe abwino.

Mwana wazaka ziwiri akachita kusamvera koma osadzudzulidwa, khalidweli likhoza kukhala lokhazikika. Popanda kulowererapo, mwanayo angapitirizebe kunyozera anthu aulamuliro pamene akukula. Mwano uwu akhoza kukachitira aphunzitsi, atsogoleri, osunga malamulo, ndiponso pamapeto pake Mulungu Mwiniwake.

Kwa makolo, nkofunika kuika malire odziwika bwino ndi kuwatsatira bwino lomwe. Chilango sichiyenera kunyalanyazidwa kapena kutengera mmene mwadzukira. Kukhala wosasinthasintha, wokhulupirika, ndi wachikondi poneneratu komanso kupereka chilango, kumathandiza ana kumvetsa kufunika kwa kumvera. Kumvera makolo kumayala maziko a moyo wonse wa kulemekeza ulamuliro wa Mulungu.

Pamene akulimbikitsa moyo womvera kwa ana akanali aang’ono, makolo amakwaniritsa udindo wao waumulungu, wotsogolera ana awo ku moyo wachikhulupiriro ndi ulemu waumulungu.

Mau a Nyengo Yake

LALIKIRA MAU

Lalikira mau; chita nao pa nthawi yake, popanda nthawi yake; tsutsa, dzudzula, chenjeza, ndi kuleza mtima konse ndi chiphunzitso. — 2 Timoteo 4:2

Mtumwi Paulo analamula Timoteo, yemwe anali mwana wake kuuzimu, kuti alalikire Mau molimba mtima, ndi chitsimikizo chonse, ndi moleza mtima. Malangizo amenewa ali ofunika chifukwa chiyani? Kodi palinso chifukwa china chakuti tilalikire? Munthu akhoza kulalikira maganizo ake, zimene amazikhulupirira, ziphunzitso za mpingo, miyambo ya anthu, nthano, ziphunzitso zonyenga, ndi zina zotero. Zimene Paulo anamulamula Timoteo zikugwirizana ndi changu chimene ayenera kukhala nacho abusa masiku ano. Lalikirani Mau opatsa moyo kuti potero miyoyo yambiri ikapulumutsidwe kumphamvu ya uchimo ndi kukhala moyo wolungama ndi waumulungu. Nzeru zozama za anthu komanso malamulo okhazikika a ziphunzitso zachipembedzo zimenezi sizimabweretsa mtendere ku moyo ndipo sizidzakonzekeretsa anthu ku moyo wosatha. Nzeru za dziko lapansi sizingapereke yankho ku zosoweka zozama za moyo.

Kupyolera mu kupusa kwa kulalikira; makamaka kulalikira za mtanda ndi Khristu wopachikidwayo kudzaonetsa njira kwa iwo amene ali kufunafuna moona mtima. Ngati inu simulalikira Mau, ndani wina amene adzatero? Ambiri amanena za ubwino wa chipembedzo chao, koma ndi ochepa chabe amene amalalikira za njira yopapatiza imene imatimasula ku ukapolo ndi kutitsogolera ku moyo wosatha.

Paulo anachenjeza Timoteo kuti idzafika nthawi pamene anthu sadzafuna kumva chiphunzitso choona komanso choonadi. Iwo adzafunafuna aphunzitsi akuti awalalikire zowakomera kuzimva ndi zosavuta kuzichita. Iwo adzasiya choonadi ndi kuchitchula kuti chili nthano chabe. Panopa tikukhala mu nthawi imeneyo.

Pali zopsinja mkati ndi kunja komwe kuti tilalikire zimene zimagwirizana ndi zofuna za anthu. Ena amafuna chiphunzitso chophweka chimene sichifuna kudzimana kulikonse. Ena amafuna kumva kuti munthu akhoza kulandiridwa ndi Mulungu komabe nkumapitiriza kuchimwa. Anthu ena amafuna kukhala ndi moyo monga mwa zofuna zathupi ndipo ali ndi mlaliki wao yemwe lamulungu amawauza kuti zonse zili bwino ndi miyoyo yawo. Kwa atumiki anzanga a uthenga wabwino: “Lalikirani Mau.”

Pamene ena akufuna kuchotsapo zina pa Mau, pali ena amene akufuna kuonjezerapo zina. Ena amafuna kuika miyezo yawoyawo pa mlingo wa chiphunzitso. Iwo amafuna kuphunzitsa malamulo a anthu. Iwo amafuna kukhazikitsa mtundu wao wa choonadi podzionetsa kuti ali auzimu kwambiri kuposa ena. Kwa atumiki anzanga a uthenga wabwino: “Lalikirani Mau.”

"Atate wathu wa Kumwamba, tikupemphani kuti mutipatse mphamvu zaumulungu kuti titumikire mwanzeru komanso mwakuzindikira. Tithandizeni kuti tibisale kuseli kwa mtanda wa Khristu ndikulalikira Mau oona a Mulungu popanda kuonjezerapo kapena kuchotsapo. Tipatseni ife chisomo ndi mphamvu kuti tikhalebe okhazikika ndi kukana zipsinjo zomwe zatizungulira. Tithandizeni kuti tikhale adindo abwino a uthenga wabwino munyengo ino. Tiloleni titsatire lamulo la Paulo ndi kulalikira Mau mokhulupirika, chita nao pa nthawi yake, popanda nthawi yake. M’dzina la Yesu. tapemphera. Amen.” ■

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE